## UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

**NYENGO MSABATAYI**


**KUYAMBIRA PA 28 OCTOBER MPAKA PA 3 NOVEMBER, 2024**

**NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI**

Tiyembekezere nyengo **ya mvula ya mabingu ndi mphepo ya mkuntho mmadera ena**. Nyengoyi idzayamba Lolemba m'madera am'zigawo za pakati ndi kumpoto ndipo idzafalikira m'madera am'chigawo cha kum'mwera pofika Lachiwiri pa 29 October 2024. Izi zikhala chonchi kamba ka dera lodzetsa mvula lomwe likuyembekezeka kukhudza nyengo ya kwathu kuno m'sabatayi. **Nyengo yotentha monyanyira ndi modetsa nkhawa** idzachepa mphamvu pofika Lachitatu pa 30 October 2024.

**NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI**

Dzuwa linaswa mtengo m'madera ambiri ndipo kunalinso kwa nyengo yotentha monyanyira. Komwe kunatentha kwambiri, pofananiza ndi mulingo okhazikika, ndi kwa Ngabu ndi madigiri opitirira +5.7°C, komanso ku Mzuzu ndi madigiri opitirira +5.0°C Loweruka pa 26 October 2024. Kwa Ngabu ku Chikwawa kunatentha ndi madigiri 42°C, pomwe ku Mangochi madigiri anafika 38°C Lachitatu pa 23 October, 2024 (Onani mapu mmunsimu)**.**




*Mapu: Mlingo wa katenthedwe pofananiza ndi mlingo wokhazikika wa 1991 mpaka 2020.*

**MALANGIZO M'SABATALI**

- ***Nyengo yotentha ndi ya dzuwa**: Tizimwa madzi pafupipafupi komanso tisamakhalitse pa dzuwa.*
- ***Mphenzi komanso Mphepo ya Mkuntho**: Tibisale pa malo otetezeka bwino kukamagwa mvula ya mabingo. Tionetsetse kuti nyumba zathu ndi zolimba bwino pamene nyengo yamvula ikuyamba.*
- **Alimi:** Alimi akulimbikitsidwa kuti apeze **ulosi wa nyengo ya dzinja la 2024/2025 wa mmaboma awo** kuti athe kupanga zisankho zoyenera pa ulimi. ([https://www.metmalawi.gov.mw/products/seasonal-climate-outlook/the-2024-2025-seasonal-climate-outlook/](https://www.metmalawi.gov.mw/products/seasonal-climate-outlook/the-2024-2025-seasonal-climate-outlook/))

## UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

***Kuti mudziwe zambiri funsani kwa:*** *The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*

**Malo osindikizira: Blantyre** **Yatulutsidwa Lamulungu pa 27 October, 2024**